Phunziro 1, July 4, 2026



# UTUMIKI WA PAULO KWA AKORINTO


“Usiku wina Ambuye anaonekera kwa Paulo m’masomphenya namuwuza kuti, “Usaope, pitiriza kuyankhula, usakhale chete. Pakuti Ine ndili nawe, palibe aliyense amene adzakukhudza ndi kukuchitira choyipa, chifukwa mu mzinda muno ndili ndi anthu ambiri.’ ”
(Machitidwe 18:9,



Kutsatira Kalata ya kwa Aroma, Makalata a kwa Akorinto ndiwo makalata atali kwambiri amene Paulo analemba.

Makalata awiri amene alipo mpaka lero analembedwa mkati mwa masabata ochepa chabe. M'menemo timapezamo malangizo othandiza pa kuthana ndi makhalidwe ovuta omwe amakhalapo chifukwa cha kusamvana pakati pa abale ndi alongo.

Kuti timvetse bwino uthenga wa makalata amenewa, choyamba tiyenera kudziwa momwe zinthu zinaliri pa nthawi imene analembedwa.





Maitanidwe a Paulo

Ulendo wopita ku Akorinto

Mzinda wa Korinto.

Akorinto

Makalata a ku Akorinto



# MAITANIDWE A PAULO

Paul, an apostle—sent not from men nor by a man, but by Jesus Christ and God the Father, who raised him from the dead (Galatians 1:1)

Kupatula atumwi khumi ndi awiri amene Yesu anawasankha, Baibulo limatchulanso atumwi ena monga Matiya (Machitidwe 1:26), Barnaba (Machitidwe 14:4), Yakobo ndi Paulo (1 Akorinto 15:7–9)

| | |
|---|---|
| Kodi Paulo anakhala bwanji mtumwi? | Muchisankho cha Yesu (Agalatiya. 1:1) |
| Anasankhidwa liti? | Kuchokera m'mimba mwa Mayi ake (Agalatiya 1:15) |
| Anaitanidwa liti? | Pa mseu wa ku damasiko (Machitidwe 22:6-7) |
| Kodi iye anali mtumwi wa ndani? | Wa kwa Amitundu (Agalatiya 2:9). |





Kuyambira pa nthawi imene adaitanidwa, moyo wa Paulo unalunjika pa Yesu. Adaganizira za Yesu, adalankhula za Yesu, ndipo ankagawana uthenga wa Yesu ndi aliyense.

Chifukwa cha ichi, kuyambira nthawi yoyamba imene adafika ku Korinto, Yesu anali pachimake pa uthenga umene iye ankafalitsa (1 Akorinto 2:2).




# ULENDO OPITA KU KORINTO

"Zitatha izi, Paulo anachoka ku Atene napita ku Korinto." (Machitidwe 18:1)

Pa ulendo wake wachiwiri wautumiki, Paulo anatsogoleredwa ndi Mzimu Woyera kupita ku Ulaya (Machitidwe 16:6–10). Kumeneko adapitikitsidwa kuchoka ku Filipi (Machitidwe 16:12, 38–39), ku Tesalonika (Machitidwe 17:1, 5, 9–10), komanso ku Bereya (Machitidwe 17:13–14)..



Ku Atene, atatha kulalikira kwa Ayuda m'sunagoge ndi kwa Amitundu pamsika, anaitanidwa kukalalikira pa Areopagi (Machitidwe 17:16–21). Ngakhale atalalikira mwaluso, ndi anthu ochepa okha amene analandira Yesu (Machitidwe 17:34).



Atachoka ku Atene, Paulo anapita ku Korinto ndipo anakakhala ndi Akula ndi Prisila. Limodzi ndi iwo ankagwira ntchito yopanga mahema (Machitidwe 18:1–3).



Monga mmene ankachitira nthawi zonse, anayamba kulalikira kwa Ayuda m'sunagoge, kenako kwa Amitundu (Machitidwe 18:4–8). Pa nthawi imene ankakhala ku Korinto, ndipo pambuyo pa 'zokhumudwitsa' zimene anakumana nazo ku Atene, Paulo anatsimikiza mtima kuti sadzadaliranso nzeru za anthu, koma azilalikira za 'Yesu Khristu, wopachikidwa pa mtanda' yekha(1 Akorinto 2:2).

# MZINDA WA KORINTO

"ngakhale kuti alipo ambiri otchedwa 'milungu' ndi 'ambuye' ambiri" (1 Akorinto 8:5).



Mzinda wa Korinto unawonongedwa kotheratu ndi Aroma mu chaka cha 146 BC. Pambuyo pake, mu 46 BC, Yuliyo Kaisara anatumiza kumeneko gulu la asilikali opuma pantchito ndi anthu omasuka kuti akakhazikike. Pofika mu 44 BC, mzindawo unali utabwezeretsedwanso bwino. Pa nthawi imene Paulo anafikako, Mzinda wa Korinto unali utakhala kale malo ofunika kwambiri ochitira malonda.



Kufunika kwa Korinto kunachokera pa malo ake omwe mzindawu unakhadzikitsidwa, KuKorinto kunali mlathu wapamtunda omwe unkalumikiza madoko awiri ofunika kwambiri pa za malonda: Lechaeum, pa Nyanja ya Gulf of Corinth; ndi Kenkereya, pa Nyanja ya Saronic Gulf.

Malonda ochuluka a ku Korinto anapatsa Paulo mwayi wogwira ntchito yopanga matenti. Koma chuma cha ku Korinto (chomwe chinkapikisana ndi cha ku Atene) chinali ndi zovuta zingapo.



Kupembedza mafano ndi chiwerewere zinali zitadzaza mzinda wa Korinto ndipo zinalowa kwambiri m'chikhalidwe cha anthu ake. Gawo lalikulu la uthenga wa Paulo kwa Akorinto linali lofuna kuthetsa mavuto amenewa, amene anayamba kulowa mumpingo.



# AKORINTO

"Usiku wina Ambuye anaonekera kwa Paulo m'masomphenya namuwuza kuti, 'Usaope, pitiriza kuyankhula, usakhale chete' " (Machitidwe 18:9)





Ayuda a ku Korinto anakana uthenga umene Paulo ankalalikira. Choncho, anakakamizika kuchoka m'sunagoge ndiukuyamba kusonkhana ndi kulalikira kwa Amitundu m'nyumba imene inali pafupi ndi sunagoge (Machitidwe 18:4–7).



"Kuipa kwa makhalidwe kumene anaona pakati pa Amitundu, pamodzi ndi kunyozedwa ndi chipongwe chimene analandira kuchokera kwa Ayuda, zinamubweretsera chisoni chachikulu mumtima. Iye anayamba kukayikira ngati kunali kwanzeru kumanga mpingo pogwiritsa ntchito anthu amene anawapeza kumeneko" (EGW The Acts of the Apostle p. 250).

Pa nthawi imeneyo, Yesu anaonekera kwa Paulo usiku m'masomphenya kuti amulimbikitse kupitiriza ntchito yake pakati pa Akorinto, ndikumutsimikizira kuti kunali anthu ambiri amene adzalandire uthengawo (Machitidwe 18:9-10).



Atalimbikitsidwa ndi masomphenya amenewa, Paulo anakhala ku Korinto kwa chaka chimodzi ndi theka (Machitidwe 18:11). Pambuyo pake, Ayuda anamupititsa Paulo ku bwalo la milandu (Machitidwe 18:12–13). Pofika nthawi imene anachoka ku Korinto, mpingo waukulu unali utakhazikitsidwa kale (Machitidwe 18:18).

# MAKALATA A KU AKORINTO

*"Abale anga, ena a ku nyumba ya Kloe andidziwitsa kuti pali mkangano pakati panu." 1 Akorinto 1:11*

## 1 Akorinto 1-6

Atamva kuchokera kwa Kuloe za mavuto angapo amene analipo mu mpingo, Paulo anawadzudzula ndi kuwaphunzitsa pa nkhani za: magawano; chiwerewere; mikangano; ndi uhule.

## 1 Akorinto 7-16

Anthu a m'banja la Kuloe anabweretsanso kwa Paulo kalata yochokera ku mpingo yokhala ndi mafunso angapo. Poyankha mafunso amenewo, Paulo anaphunzitsa pa nkhani za: ukwati; chisudzulo; kusakwatira; zakudya zoperekedwa nsembe kwa mafano; zochitika pa nthawi ya kulambira; kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za Mzimu; ndi kuuka kwa akufa.

## 2 Akorinto

Iyi ndi kalata yachiwiri imene yanasungidwa mpaka lero, ngakhale kuti Paulo analemba makalata ena angapo (mwina asanalembedwa makalata awiri amene alipowa, kapena analembedwa pakati pa makalata awiriwa). Iye anayamikira Akorinto chifukwa cha mmene anathetsera mavuto ena, koma anawalimbikitsa kuti aziyang'ana dziko kudzera m'maso a Uthenga Wabwino, kupewa kutengera chikhalidwe cha anthu owazungulira.









"Atumiki a Mulungu m'mizinda ikuluikulu sayenera kutaya mtima chifukwa cha kuipa, kusalungama, ndi kuwonongeka kwa makhalidwe kumene amakumana nako pamene akuyesetsa kulalikira Uthenga Wabwino wa chipulumutso. Ambuye akufuna kulimbikitsa mtima wa wogwira ntchito aliyense wotere ndi uthenga womwewo umene adapereka kwa mtumwi Paulo m'mzinda woipa wa Korinto wakuti: 'Usaope, koma lankhula ndipo usakhale chete; pakuti Ine ndili nawe, ndipo palibe amene adzakuvulaze, chifukwa ndili ndi anthu ambiri mu mzinda uno.' (Machitidwe 18:9–10). … […]

M'mzinda uliwonse, ngakhale utadzaza ndi ziwawa komanso umbanda, muli anthu ambiri omwe ndi chiphunzitso choyenera akhoza kuphunzira kukhala otsatira a Yesu. Zikwi zambiri motero zikhoza kufikiridwa zambiri zingafikiridwe ndi choonadi chopulumutsa ndi kutsogoleredwa kulandira Khristu monga Mpulumutsi wawo wa iwo eni."

EGW (Prophets and Kings, p. 277)